Mutu Wachisanu

Chipangano Chosungira (Chipangano cha Nowa)

Mu phunziro la mapangano lino, tikuona ntchito za Mulungu Mlengi pokhudzana ndi munthu cholengedwa chake. Gwero lokhalo la chidziwitso limapezeka m'mavumbulutso a Mulungu mwa Iye mwini m'Malemba Oyera. Muno timapeza mapangano asanu ndi atatu ofunika kwambiri omwe Mulungu anachita ndi anthu, mitundu, ndi magulu a anthu. Mulungu anakhazikitsa mfundo zimene zinafotokoza zolinga zake pa dziko lonse lapansi. Chifukwa chakuti Mulungu amalamulira monga Mfumu pa chilengedwe chake chonse, yankho labwino la munthu ndilo kulandira ndi kumvera zimene Mulungu wanena.

M'mutu wachitatu, chipangano choyamba, chomwe ndi Chipangano cha Ulamuliro, chinatanthauzira ubale wa munthu ndi dziko lake. Mulungu anamupanga munthuyo kukhala wotha kusankha kuti athe kuyendetsa ulamuliro wake. Chisankho chimodzi cholakwika chinapangitsa kuti anthu agwe m'njira yowopsa. Chipangano cha Ulamuliro chinaswa, ndipo Mulungu anakumana ndi anthu ochimwawo ndi chiweruzo.

Mwachifundo ndi chisomo, Mulungu amalonjeza chipulumutso kwa munthu wogwayo. Chipangano cha Chipulumutso chinalengezedwa kuti chibweretse chiyembekezo. Adamu ndi Hava anachotsedwa m'munda wawo wangwiro wa Edene kuti akagwire ntchito ndi kudzaza dziko lapansi. Zonsezi zinasimbidwa mu Genesis 1-3.

Kusamvera kwa Hava ndi Adamu kunabala zipatso msanga mwa mwana wawo woyamba, Kaini. Mulungu analandira nsembe imene Habila anapereka. Koma sanalandire nsembe ya Kaini, zomwe zinapangitsa Kaini kukwiya, mkwiyo woti mpaka anapha mchimwene wake. Kupyolera mu mbandayo, Kaini anayamba njira yaubve yomwe inafika poipa kwambiri pamene banja la anthu linkachuluka. Genesis 4 imasimba za abale oyambirira amenewa.

Tikadutsa msanga mwa Genesis mutu 5, tikuona kuti anthu m’zaka zoyambirira zimenezo ankakhala moyo wautali. Mwa amuna naini kuyambira Adamu mpaka Nowa, asanu ndi awiri anakhala zaka zopitirira mazana asanu ndi anayi (900), ndipo anabala ana. Akuti pofika nthawi ya Nowa, patapita zaka chikwi chimodzi, mazana asanu ndi limodzi mphambu makumi asanu ndi limodzi kudza zisanu (1,656) kuchokera pamene dziko linalengedwa, chiwerengero cha anthu padziko lonse chikadapitirira mabiliyoni asanu ndi awiri (7 billion)! Kuchokera pa chigumula, patatenga zaka masauzande ambiri, mpaka mu 1987, kuti dziko lifike pa anthu mabiliyoni asanu! Akuti pofika chaka cha 2015 chiwerengerocho chidzafika mabiliyoni asanu ndi limodzi. Choncho, chiwerengero cha anthu nthawi imeneyo chinali chochuluka kuposa masiku ano. Pa kukwera kwa chiwerengeroku, m’zaka makumi ochepa zikudzazi, chiwerengero cha anthu chidzafika pamlingo wa nthawi ya Nowa. Kodi izi zingakhale m’modzi mwa mikhalidwe imene Yesu anaitanthauza pamene anati, "Monga masiku a Nowa analili, kotero kudzakhala kudza kwa Mwana wa Munthu...?"

M’mutu uno tiona Mulungu akugwira ntchito mu Chipangano Chosungira. Chiyero cha Mulungu chinakhumudwa ndi kuipa kwa anthu. Njira yokhayo imene inatsala inali chiweruzo: kuyeretsa dziko ndi kuyambanso kwatsopano. Tiona Chipangano Chosungira m’magawo asanu kutengera nkhani ya mu Genesis 6:1 mpaka 9:17. Tiona Mulungu akuchita ndi mkhalidwe wa anthu ogwa, akufotokoza zigawo za dongosolo Lake losunga otsala. Kenako tiona Mulungu akusunga chilengedwe Chake, akupulumutsa olungama ndi kukhazikitsa chipangano Chake chachitatu.

Gawo Loyamba

MULUNGU AKUYANG’ANIZANA NDI KUKHALA WOIPA KWA MUNTHU

Munthu ayenera kudabwa ndi chisomo komanso chifundo cha Mulungu pakupanga munthu m’chifaniziro Chake kuti akhale bwenzi Lake, akudziwa kuti ufulu wosankha wa munthu

sudzagwiritsidwa ntchito mwanzeru nthawi zonse. Ndipo cholengedwa chomwe Mulungu anachipangira kuti chikhale bwenzi Lake chinakhala mdani Wake. Kusamvera ndi kupanduka kunachotsa munthu kwa Mulungu ndi kumuponya m'kudzimana, kuchoka ku kuwala kupita ku mdima. Malipiro a uchimo ndi imfa. Mkwiyo woyera wa Mulungu unayenera kukhutsidwa, n'chifukwa chake kunabwera chigumula.

N'zochititsa chidwi kufotokozedwa kwa mikhalidwe ya dziko komanso yankho la Mulungu mu Genesis 6:1-7.

1. *Ndipo kunali, pamene anthu anayamba kuchuluka pa dziko lapansi, ndipo anawabalira ana aakazi,*

2. *Kuti ana a Mulungu anaona ana aakazi a anthu kuti anali okongola; ndipo anadzipatula akazi mwa onse amene anawasankha.*

3. *Ndipo Yehova anati, Mzimu wanga sudzalimbana ndi munthu nthawi zonse, chifukwa iye alinso thupi: koma masiku ake adzakhala zaka zana limodzi mphambu makumi awiri.*

4. *M'dziko lapansi munali zimphona masiku amenewo; komanso pambuyo pake, pamene ana a Mulungu analowa kwa ana aakazi a anthu, ndipo anawabalira ana, iwo omwewo anakhala anthu amphamvu a kalekale, anthu otchuka.*

5. *Ndipo Mulungu anaona kuti kuipa kwa munthu kunali kwakukulu pa dziko lapansi, ndi kuti kulingalira konse kwa maganizo a mtima wake kunali koipa kokha nthawi zonse.*

6. *Ndipo Yehova anachita chisoni kuti anali atapanga munthu pa dziko lapansi, ndipo zinampweteka m'mtima mwake.*

7. *Ndipo Yehova anati, Ndidzafafaniza munthu amene ndinalenga pa dziko lapansi; munthu, ndi chirombo, ndi chokwawa, ndi mbalame za m'mlengalenga; pakuti ndichita chisoni kuti ndinazilenga.*

Pano tiyenera kupenda MIKHALIDWE ya anthu imene inatsogolera ku Chipangano Chosungira.

MKHALIDWE WA ANTHU (SOCIAL CONDITION) unachititsa kuti Wamphamvuyonse achitepo kanthu. Mulungu ataona kuti si bwino kuti Adamu akhale yekha, anamulengera mkazi mmodzi. Ndipo Adamu anati mwamuna adzasiya atate wake ndi amayi wake ndipo adzaphatikizana ndi mkazi wake (Genesis 2:24). Choncho tikudziwa kuti mwamuna mmodzi ndi mkazi mmodzi kwa moyo wawo wonse ndicho chifuniro cha Mulungu.

Pofika masiku a Nowa, lamulo limeneli linaphwanyidwa kwambiri. Amuna ankadzitengera akazi momwe angafunire. Kusasamala koteroko kunadzetsa chiweruzo cha Mulungu. Yesu analankhula za masiku amenewo: "...ankadya ndi kumwa, akwatira ndi kukwatiwa..." Mateyu 24:38. Makhalidwe a anthu anali otsika kwambiri.

N'zamanyazi kuti anthu amene poyamba analengedwa m'chifaniziro ndi m'mawonekedwe a Mulungu woyera mtheradi anasangalala m'nyansi za uchimo. Anakana kotheratu kuitana kwapamwamba kwa Mulungu ndipo anatsikira pamlingo wa zilombo. Mulungu anaona kukula kwa kuipa kwa munthu ndipo anati mu Genesis 6:7, "...Ndidzafafaniza munthu amene ndinalenga pa dziko lapansi..."

Chifukwa cha kukula kwa chiwerengero cha anthu, titha kunena moyenera kuti chisonkhezero choipa cha mbadwa za Kaini chinafalikira kwambiri. Makhalidwe a anthu anali oteropa moti n'kosatheka kusintha. Njira yokhayo imene inatsala kwa Mulungu inali yochita chiweruzo.

MKHALIDWE WAUZIMU unalimbikitsa Mulungu kupulumutsa otsala. Popeza anthu amapanga gulu lomwe lili ndi kuthekera kwauzimu, anthu akakhala oipa m'dera lina la moyo, zimakhudza madera onse. Kuipa kwa makhalidwe kunali chifukwa cha kupanduka kwa uzimu.

Kusakanikirana kwa ana a Mulungu ndi ana aakazi a anthu kukusonyeza momwe anthu anatalikirana ndi Mulungu. Genesis 6:8 ndi vesi lotsitsimutsa ndipo nthawi yomweyo ndi lokhumudwitsa: "Koma Nowa anapeza chisomo pamaso pa Yehova." Ngati, monga tanenera kale, chiwerengero cha anthu chinafika mabiliyoni asanu ndi awiri ndipo munthu mmodzi yekha "anapeza chisomo pamaso pa Yehova," ndiye kuti mkhalidwe wauzimu unali wotsika mofanana ndi makhalidwe a anthu.

Anthu anakhulupirira Mulungu nsana ndipo anatsimikiza mtima kutsatira njira zawo. Kusanthula kwa Ambuye pa mkhalidwewo kwaperekedwa mu Genesis 6:12: "Mulungu nayang'ana dziko lapansi, ndipo, taonani, linali lovunda; pakuti anthu onse anadziipsa njira yawo pa dziko lapansi."

Lingaliro lonyenga lofuna kukhala ngati Mulungu, limene chinjoka chinapereka kwa Hava m'Munda wa Edene, linapangitsa mkhalidwe woipa wauzimu wotalikirana kotheratu ndi Mulungu. Satana anakwaniritsa cholinga chake chotsegula maso a Hava ku zoipa. Iye anakopeka nazo ndipo anagwera mu msampha wa Satana. Iye anatchera msampha wake mwaluso kwambiri moti pofika nthawi ya Nowa onse kupatula Nowa anali atakodwa. Ndipo Mulungu anakana kukhala ndi anthu amene anali atawalenga. M'malo mwake Iye analumbira kuti adzawawononga.

MKHALIDWE WA MAKHALIDWE (MORAL CONDITION) unalimbikitsa Mulungu kuweruza. Pachilengedwe choyambirira Adamu anali wangwiro m'thupi, moyo ndi mzimu.

Mtima wa Adamu unapangidwa kuti uzilankhulana ndi Mlengi wake, ndipo ankatha kutero, chifukwa munthu asanachimwe anali woyera, monga Mulungu. Popeza Mulungu anapanga munthu m'chifaniziro Chake, munthu anali ndi ungwiro wa makhalidwe ndanso ufulu wa makhalidwe. Komabe, pokhala ndi makhalidwe, munthu anali wofooka, kutanthauza kuti, akasankha kumvera chifuniro cha Mulungu kapena kusamvera. Chilichonse chomwe munthu angasankhe, Mulungu anali atatsimikiza kale zotsatira zake. Mulungu analamula kuti kusamvera kudzabweretsa imfa kwa Adamu. Poyankha chinyengo cha chinjoka, Hava adadya chipatso choletsedwa ndipo imfa inadza.

Mwa mawu a mu Genesis 6:5 titha kuona mkhalidwe wa makhalidwe: "Ndipo Mulungu anaona kuti kuipa kwa munthu kunali kwakukulu pa dziko lapansi, ndi kuti kulingalira konse kwa maganizo a mtima wake kunali koipa kokha nthawi zonse."

Munthu atangoyamba kusamvera, msewu unali wotsika moti tsiku lililonse liŵiro linkawonjezereka mpaka kufika pamene panalibe pobwerera. Dziko limene linali liyenera kukhala losangalatsa. Kwamunthu, mudzi unasanduka mbewera ya chiwerewere, kuipa, ndi chiwawa. Chisangalalo chinali chinthu chofunika kwambiri choti achitsate, ndipo moyo unalibe mtengo. Panalibe chidwi ndi cholinga cha m'tsogolo. Onse ankakhala moyo wa nthawi yomweyo ndipo anadzimira m'zilakolako za thupi, popanda kuyembekezera kukumana ndi zoopsa za moyo wosatha. Ndipo Mulungu analumbira kuti achithetsa zimenezi.

CHIKHALIDWE CHA CHIWERUZO chinapangitsa Mulungu kuti awononge dziko. Kuwerenga kuti "Yehova anamva chisoni kuti adalenga munthu," kumadzutsa mafunso mpaka titasanthula tanthauzo la mawu oti kulapa (chisoni) mu Chihebri. Tanthauzo lake ndi kuusa mofatsa kapena molemedwa. Mulungu anali ndi chisoni chachikulu chifukwa chakuti anthu anapatuka pa mmene Iye anawalengera kuti akhalire. Tiyenera kukumbukira kuti chosankha cha

Mulungu cholenga munthu chinachokera mwa kufuna kwake. Sanakakamizidwe kulenga munthu. Komanso sanakakamizidwe kulenga munthu kukhala mfulu woti azidzisankhira yekha zochita. Zolengedwa zina zonse zimatsatira malamulo achibadwa omwe anaikidwamo kale. Munthu yekha ndiye amasankha.

Izi zimakhala zovuta chifukwa chakuti munthu akhoza kusankha choipa. Akhoza kusankha kusamvera Mulungu. M'zaka chikwi chimodzi ndi mazana asanu ndi limodzi mphambu makumi asanu ndi limodzi (1,656), mtundu wonse wa anthu unasankha zoipa kupatula banja limodzi la anthu asanu ndi mmodzi mphambu awiri (8). Nowa yekha ndiye anali wolungama. Choncho, njira yokhayo imene inatsala kwa Mulungu inali chiweruzo, chomwe pa nthawiyo chinali chiwonongeko. Mulungu anati, "Ndidzawononga munthu amene ndinamulenga pamaso pa dziko lapansi..."

Ngakhale kuti mkhalidwe woopsawu unakakamiza Mulungu kuchita zinthu mwankhanza chonchi, pangano lake ndi Nowa linaonetsa chilungamo chake. Mulungu adalankhula ndi Nowa ndipo anati mwa Genesis 6:18,19: "Koma ndidzapanga pangano langa ndi iwe; ndipo udzalowa m'chingalawa, iwe, ndi ana ako, ndi mkazi wako, ndi akazi a ana ako pamodzi ndi iwe. Ndipo pa chamoyo chilichonse cha zamoyo zonse, udzalowetsa m'chingalawa ziwiri za mtundu uliwonse, kuti zikhale ndi moyo pamodzi ndi iwe; zikhale zamwamuna ndi zazikazi."

Chifundo cha Mulungu chimawala ngati nyali ya paphiri. Chili ngati muuni wa kuwala m'usiku wamdima. Nowa ndi banja lake anayenera kukhala opitiliza mtundu wa anthu. Pangano limeneli moyenera limatchedwa Pangano la Chisungiko. Mulungu anasunga otsala, anthu asanu ndi mmodzi mphambu awiri, kaamba ka chiyambi chatsopano. Mulungu anasunganso chachimuna chimodzi ndi chachikazi chimodzi cha nyama zonse ndi mbalame. Pa nyama zina zoyera, zisanu

ndi ziwiri zinasungidwa. Chingalawa chomwe Nowa anayenera kumanga chinali njira imene Mulungu anawasungira.

Ena angathe kuona mchitidwe wa Mulungu wowononga kukhala wankhanza. Tisanaganize choncho, tiyenera kuganizira chibadwa cha Mulungu chomwe khalidwe lake lalikulu ndi chiyero. Tikaganizira chiyero chake, titha kumvetsetsa msanga kuti kulengeza kwake koti awononga munthu sikuli koyenera kokha, koma ndi chinthu chomwe chibadwa chake chimafuna.

M'zochita zake za chiweruzo, Mulungu akhoza kukhululukira anthu pamene avomereza machimo awo, kusamvera kwawo, kuukira kwawo, ndipo n'kupempha chikhululukiro.

Choncho, mikhalidwe ya kachezedwe, yauzimu, yakhalidwe, ndi yachiweruzo imabwera pamodzi pofuna kufotokoza kufunika kwa Pangano la Chisungiko. Sitiyenera kuiwala mawu a Yesu pamene anati, "Monga masiku a Nowa analili, kotero kudzakhala kufika kwa Mwana wa munthu."